

Ulemu kwa Atate



Uthengawu unaperekedwa ndi Mlaliki (Muballigh) wa Dawat-e-Islami komanso ndimembela wa Shura, Haji Abu Madani Abdul Habib Attari (مَدَائِلَةُ الْعَنَانِي), pa tsiku la 1 Safar-ul-Muzaffar 1442 AH kulingana ndi pa 18 September 2020 pa Msikiti wa Faizan-e-Ala Hazrat, Manzoor Colony, Karachi. Izi zasonkhanitsidwa ndi ya "Malfuzaat Ameer-e-Ahl-e-Sunnat" ya Al-Madinat-ul-Ilmiyyah.

**Zaperekedwa ndi: Al-Madinat-ul-Ilmiyyah
(Dawat-e-Islami)
Malo Ofufuzira za Chisilamu.**

باپ کی عظمت و شان

Ulemu kwa Atate

Zankatimu

Ulemu kwa Atate	1
Ubwino wolembe Mawu wonfunira zabwino Mtumiki ﷺ	1
Onesetsani kuchita chikondi kwa Mayi anu komanso chimodzimodzi Atate anu.	1
Kutumikira Atate kunapangitsa mwana kukhala wopambana	2
Photo yotumikira a Mayi.....	4
Ngakhale Mulingo wochepa wa halal umakhala ndi madalitso a mbiri.....	5
Atate ali ngati mitengo yomwe imapereka nthunzi.....	6
Omwe amatumikira makolo awo ndi odala	7
Nkhani yonvetsa Chisoni ya Atate.....	8
Makolo amakhala ndi moyo chifukwa cha ana awo	9
Mwana yemwe anasiya atate ake.....	10
Musayiwale chifundo cha atate anu.....	11
Mumakolola zomwe mwazala	12
Ubwino wa atate potengera M'mahadith.....	14
Mphoto ya hajj yolandiridwa pa kuyang'ana kulikonse.....	16
Momwe mungasangalatse makolo omwe anamwalira.....	16
Momwe mungawachitire Du'a Makolo	17
Chithandizo chowonjezera rizq.....	18
Chifukwa choyambitsa kusowa kwa Madalitso mu rizq.....	18

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ ط بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

Ulemu kwa Atate¹

Ubwino wolemba Mawu wonfunira zabwino Mtumiki ﷺ

Mtumiki Wachifundo ﷺ anati, “Aliyense amene anangalembe mawu (ṣalāt) m’buku; angelo adzapitiriza kumupempherera chikhululukiyo malinga ngati mawuwo angakhalabe mmenemo.”²

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Onesetsani kuchita chikondi kwa Mayi anu komanso chimodzimodzi Atate anu

Kutumikira makolo a munthu ndi dalitso wawukulu. Komabe, ena mwa ife sitiwatumikira ndipo timaphonya madalitso omwe amabwera ndi izi, kulephera kuzindikira kukula kwa anthu awa. Nthawi zambiri timanva za amayi ndi momwe mapemphero awo ali ngati kamphepo kaku Paradiso. Paradiso ili pansi pa mapazi a amayi.³ Komanso, mapazi a amayi afotokozedwa ngati khomo la Paradiso.⁴

Mosakayikitsa, palibe amene angafanizidwe ndi amayi ndipo palibe wina m'malo mwawo m'dziko lino. Komabe, zikafika pa kutumikira, kulemekeza, ndi kupereka ulemu kwa atate, mulingo ofanana wa chidwi sulephereka kuperekedwa. Chikondi

¹ Ulaliki uwu unaperekedwa ndi Abū Madani Abd al-Habib Attari pa 1st Şafar 1442 AH/ 18th September 2020, ku Faizan-e- Ala Hazrat Masjid, Manzur Colony, Karachi. Nsonkhano unachitika ncholinga chofikitsa photo kwa malemu Bambo ake. Pamene ulaliki uwu umawulutsidwa pa Madani Channel, Mawlana Ilyas al-Qadiri دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةُ anampempherera komanso anafunutsitsa kuti ulalikiwu uchitidwe kukhala Buku ndikulifalitsa ngati kabuku. (Malfuzat Amir Ahl al-Sunna Department)

² Al-Mu‘jam al-Awsat: Hadith 1835

³ Musnad al-Shihāb: Hadith 119

⁴ Durr al-Mukhtār, vol. 9, p. 404

kwa atate sichisonyezedwa kwambiri, ngakhale ali ndi udindo wapadera komanso wofunika kwambiri m'miyoyo yathu.

Kutumikira Atate kunapangitsa mwana kukhala wopambana

Munthu wina anali ndi ana aamuna anayi. Atadwala, mmodzi wa iwo anapereka pemphero lachilendo kwa abale ake. Iye anati: “Inu atatu samalirani atate athu. Mudzapeza mphotho yayikulu, koma chifukwa cha izi, musatenge gawo lililonse la cholowa. Kapena mungandipatse ine udindo wokuwasamalira. Ine ndidzawatumikira ndipo pamboyo pake sindidzatenga gawo lililonse la cholowa.”

Ndi n'gwirizano wachilendo bwanji! Ndani amakana ndalama masiku ano? Komabe, M'baleyo anadziwa mphotho yomwe idzabwera chifukwa chotumikira atate ake. Abale atatuwo anayankha kuti, “Chingakhale chabwino n'chiyani kuposa ichi? Iwe usamalire atate athu ndipo usatenge gawo lililonse la cholowa.

” N'gwirizano umenewu unakhazikika, ndipo mwanayo anatumikira atate ake mpaka atatewo anamwalira. Mwana wodziperekayo sanatenge gawo lililonse la cholowa, monga momwe analonjezera.

Chotsatira chinali chani? Usiku wina, analota maloto omwe ananva mawu akuti,

“Pita kumalo akuti-ndi-akuti. Kumeneko, udzapeza ndalama zagolide 100. Zitenge.”

“Kodi muli madalitso mwa izo?”, iye anafunsa. Mawuwo anati ayi. M'mawa mwake,

anafotokozera nkazi wake kuti, “M'maloto anga, ndauzidwa za malo omwe kuli ndalama zagolide 100. Sindinazitenge chifukwa zilibe madalitso.” Mkazi wake anadabwa: “Ndiwe munthu wodabwitsika! Choyamba, unasiya cholowa chako ndipo sunatenge gawo limodzi. Tsopano, wapatsidwa ndalama zagolide! Ndife osawuka ukanayenera kuzitenga!” Iye anayankha kuti, “Sindikufuna chuma chomwe chilibe madalitso mwa iwo.”

Usiku wotsatira, anawonetsedwa malo m'maloto ake ndipo anawuzidwa kuti, “Palindalama zagolide 10 pamalo akuti-ndi-akuti. Pita ukazitenge.” Anafunsanso

kuti, “Kodi muli madalitso?” Yankho linali lakuti, “Mulibe madalitso.

”M'mawa mwake, anawuza nkazi wake za maloto achiwiri amenewa. Nkazi wake anafuwula, “Zodabwitsa bwanji! Kuchokera pa ndalama 100 kufika pa 10 - ukanayenera kutenga 10 imeneyo!” Iye anatsimikiza kuti, “Ngati mwa izo mulibe madalitso, sindikuzifuna.”

Usiku wachitatu, anawonetsedwa malo omwe panali ndalama imodzi yagolide, ndipo anawuzidwa kuti ayitenge. “Kodi muli madalitso mwaiyo?” anafunsa. Analandira yankho lakuti inde.

Usiku wachitatu, anawonetsedwa malo omwe panali ndalama imodzi yagolide, ndipo anawuzidwa kuti ayitenge. “Kodi muli madalitso mwa iyo?” anafunsa. Analandira yankho lakuti inde. M'mawa mwake, anapita kumalo omwe anawawona m'maloto ake ndipo anabweretsa ndalama ija ya golide. Anayigwiritsa ntchito pogula nsomba ziwiri za banja lake, akuganiza kuti, “Ngati palibe china chilichonse, ndikhoza kuwapatsa chakudya chabwino.” Pamene anafika kunyumba ndi kudula nsomba zija, anapeza ngale (pearl) n'kati mwa iliyonse. Popeza izi zinali zosowa kwambiri komanso zapadera, anaziyika pambali kuti azisunge bwino

Tsiku lomwelo, nfumu ya dzikolo inalamula kuti ikufuna ngale ya ntundu wapadera.

Oyimira nfumu anayendera ogulitsa miyala yonse yantengo wapatali mu nzindowo, koma palibe amene anali nayo yoyenera. Pambuyo pake, ananva kuti munthu wina n'dera lina anapeza ngale m'nsomba, zomwe palibe amene anaziwonapo kale. Atamupeza ndi kuziwona, anati, “Iyi ndiyo ngale yomwe nfumu ikufuna.”

Inawonetsedwa kwa nfumu, yomwe inati, “Inde, iyi ndiyo.” Ntengo wa ngaleyo unakambidwa, ndipo popeza katundu ankanyamulidwa pa mabulu ndi akavalo m'mbuyomu, munthuyo anati, “Ngale iyi idzakudyerani abulu 30 odzaza ndi golide.” Nfumu inali ndi abulu 30 odzaza ndi mitolo ya golide ndipo inagula ngale ija kwa munthuyo. Ona mulingo wa chuma chomwe chinachokera ku n'dalitso la ndalama imodzi ya golide, ndipo zimenezo zinali pambuyo pogulitsa imodzi mwa ngalezo.

Nfumu inatenga ngale ija kupita nayo kwa katswiri wa nkhaniyi. Katswiriyo anati,

“Ngale imodzi yokha siyingatulutse kukongola kwake kwenikweni. Ngale yachiwiri ya ntundu womwewo ikapezeka, m'pamene kukongola kwake kwenikweni kudzadziwika.” Nfumu inalengeza kuti, “Peza ngale ina, ngakhale itadya ntengo wowirikiza kawiri.” Kufunafuna ngale ina kunayamba, koma siyinapezeke kulikonse. Pambuyo pake, anthu anabwerera pakhomu la munthu yemweyu ndipo anafunsa kuti, “Kodi uli ndi ngale ina ngati iyi?” Iye anawulula kuti, “Inde, ndili ndi ngale ina ngati iyi, koma ikudyerani ntengo wowirikiza kawiri.” Anagula ngale yachiwiri ija kwa iye posinthanitsa ndi abulu 60 odzaza ndi golide. Kuchokera pa chochitika ichi, osati tikuphunzira kufunika kotumikira atate a munthu kokha, komanso kuti chuma chochepe cha halal chomwe chili ndi madalitso ndi chabwino kwambiri kuposa chuma chambiri chomwe chili cha haram komanso chopanda madalitso. Mulimonsemo, chifukwa mwanayo anatumikira atate ake, Allah Wamphanvu zonse anamupatsa chuma chochokera kuzinthu zosawoneka

Photo yotumikira a Mayi

Fanizo lina lodziwika bwino lafotokozedwa mu Quran yopatulika, mu Sūrat al-Baqara. M'chiarabu, liwu loti baqara limatanthawuza ng'ombe. Sūrah imeneyi ikutchula nkhani ya ng'ombe yomwe inali yokwera ntengo kwambiri padziko lonse lapansi. Anthu a nthawi imeneyo anayigula podzaza khungu lake ndi golide, ndipo inaperekedwa kwa mnyamata yemwe anatumikira ndi kunvera amayi ake. Chifukwa cha kudzipereka kwake komanso kunvera amayi ake, Allah Wamphanvu zonse anamupatsa ng'ombe yomwe inalibe ina yofanana nayo padziko lonse lapansi.¹

Ziphunzitsa zoti tiphunzire kuchokera m'mafanizo awa ndi zantengo wapatali kwa makolo komanso ana. Nthawi zambiri makolo amati akufuna kusiya zinthu zambiri kwa ana awo. Mumagwira ntchito chifukwa cha ana anu, mumawamangira

¹ (Tafseer Sawi, Gawo 1, Al-Baqarah, pa vesi 71, vol. 1, p. 75) kuti muphunzire zokhuza Fanizo la mu Qurani komanso ndi maphunziro ofunika, chonde adziwitseni za buku la “Quranic Wonders”, lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. (Nthambi ya zolankhula za Ameer of Ahl al-Sunnah).

nyumba, ndipo mumawakhazikitsira mabizinesi. Komabe, kodi simuganiza ngati zomwe mukupezera ana anu ndi halal kapena haram? Kodi simuyima kaye ndikuganizira za ntundu wa malele omwe mukuwapatsa? Kumbukirani! Ngati musiya chuma kwa ana anu koma osawapatsa malamulo abwino, adzagwiritsa ntchito chumacho kuchita machimo. Chilango cha izi chidzakugwerani inu, popeza ndinu amene munasiya chumacho kwa iwo.

Zalankhulidwa kuti ‘Umar b. ‘Abd Al-‘Azīz رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anali ndi chuma chochepa kwambiri pamene amachoka m'dziko lino. Wina anati kwa iye, “Simunasiye chilichonse kwa ana anu.” Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anapereka yankho labwino kwambiri. Anati: “Ngati ana anga sakumunvera Allah Wamphanvu zonse, si bwino kuwasiyira chilichonse, chifukwa adzachigwiritsa ntchito pa zinthu zolakwika. Ngati amamunvera Allah Wamphanvu zonse, Iye adzawapatsa kuchokera ku chuma Chake chosawoneka, adzawapatsa zokwanira, ndipo adzadalitsa riziki yawo.¹

Ngakhale Mulingo wochepe wa halal umakhala ndi madalitso a mbiri

Tiyeni pano tikambirane zinthu Ziwi choyamba, tili ndi ana olungama omwe amagwiritsa ntchito bwino chuma chomwe makolo awo anawasiyira, ndipo chachiwiri, tili ndi chuma cha halal. Ngakhale chuma cha halal chikhale chochepe, Allah Wamphanvu zonse amayika madalitso mu mlingo woche pawo chifukwa cha banjalo. Pali zitsanzo zambiri padziko lapansi pomwe mamiliyoneya amasiya mabizinesi akuluakulu kwa ana awo, omwe amapangira zoyipa ndikupangitsa bizinesiyo kulephera kutukuka mwachangu. Kumbali inayi, munthu wosawuka akhoza kumwalira pomwe ana ake ali olungama. Allah Wamphanvu zonse kenako amawadalitsa iwo ndi chuma chawo kotero kuti amaposa atate awo mu Malonda.

Munthu ayenera kupempha riziki ya halal kwa Allah Wamphanvu zonse, kunena kuti, “O Allah Wamphanvu zonse! Chilichonse chomwe mungandipatse, chipangitseni kukhala chololedwa (halal), chodzaza ndi madalitso, chodzaza ndi zabwino, komanso chodzaza ndi ntendere!” Ngakhale chuma cha halal chomwe

¹ Ihya' al-'Ulum, vol. 3, p. 288

munthu ali nacho chikhale chochepa, chimakhala ndi madalitso osaneneka. Mamiliyoneya ambiri amadwala matenda omwe amatanthawuza kuti sangathe kugona usiku wonse, pomwe munthu wosawuka yemwe amagulitsa pamalo ogulitsira amagona mwantendere usiku, amapemphera kasanu pa tsiku, ndipo ana ake ndi onvera. Izi zikusonyeza kuti bata la m'ntima ndi lomwe lili lofunika kwambiri, osati ndalama.

Atate ali ngati mitengo yomwe imapereka nthunzi

Atate ali ngati ntengo womwe umapereka nthunzi kwa ana ake ndipo umapirira kutentha kwa dzuwa iyemwini. Amagwira ntchito usiku ndi usana kuti ana ake adye mwa ntendere. Titha kukhala osazindikira, koma atate amasiya zofuna zawo kuti atipatse zofunika komanso kukwaniritsa zokhumba zathu. Pamene mwana awumirira kugula chinachake, atate amapita mopitirira bajeti yawo kuti amusangalatse mwana wawo. Izi ndi zomwe atate anga anandichitira, komanso zomwe atate anu amakuchitirani kupirira kuzovuta kuti atipatse zo pepuka . Ngati mutakhala panso pa ntengo, mudzapeza kuti mwakhala nthunzi pozizira. Koma kuchokera pamwamba pa ntengowo umakhala wotentha kwambiri, chifukwa umatenga kuwotcha konse kwa dzuwa pa iwo wokha. Atate anu ndi dalitso lalikulu lomwe mwapatsidwa ndi Allah Wamphanvu zonse. Ndi atate anu omwewo anakugwirani dzanja ndikukuphunzitsani momwe mungayendere. Ndi atate anu omwewo nthawi zonse amafuna kuti mupambane. M'dziko lino, ambiri amakhala ndi nsanje ndipo amadana ndikuwona ena akupita patsogolo. Koma atate anu ndi munthu wapadera yemwe amakhala ndi chimwemwe pamene mukupambana, chifukwa n'gwirizano pakati pa atate ndi ana ake ndi wopanda dyera. Iye adzapirira ndi mantha, koma sadzalola ana ake kukhala amantha. Ngati mwakhala ofowoka kapena mukukumana ndi zovuta, atate anu adzakulimbikitsani ndikunena kuti,

“Usadandawule, ndilipo chifukwa cha iwe”, ngakhale atakhala akudandawula iwo mwini. Akhoza kukhala pa nkhwawa yayikulu, koma salola aliyense panyumba kudziwa zamavuto omwe akukumana nawo. Amadziwa kuti ngati awuza nkazi wawo, nayenso adzakhala ndi nkhwawa, choncho palibe phindu lowapatsa nkhwawa. Choncho, amapirira wokha, nthawi zina amatenga ngongole, amakhala moyo wovuta, koma salola kuti vuto lililonse ligwere ana awo.

Omwe amatumikira makolo awo ndi odala

Nthawi imafika yoti mwanayo amakula ndipo atate amakalamba. Tsopano, ndi nthawi ya mwanayo kusamalira atate ake. Kumbukirani, ngakhale titatumikira makolo athu moyo wathu wonse, sitingathe kubwezera chifundo ndi kudzipereka kwawo. Anatinyamula pamene sitinkatha kuyenda kapena kudzidyetsa tokha. Anali iwo omwe anatilera pamene sitinkatha kutero. Anali makolo athu omwe anadzipereka ndi kutilera kuti tikhale anthu amphanvu omwe tili lero. Tsopano popeza ndi nthawi yathu yowatumikira, tiyenera kuchiwona kukhala chinthu cha ulemu komanso kuwatumikira ndi ntima wonse.

Odala ndi omwe amatumikira makolo awo. Makolo ambiri sapereka mwayi umenewo, chifukwa amakhala moyo wawo wonse akusamalira ana awo ndikuchoka m'dziko lino popanda aliyense kuwasamalira pobwezera. Ena amati sanakhalepo ndi mwayi wosamalira makolo awo. Taganizzni; atate anu amakupatsani zofunika ndipo amayi anu amakutsanulirani chikondi mpaka kumapeto, ndipo anachita izi kwambiri, sanatipatse mwayi wowatumikira pobwezera, mulingo wawo wa chikondi unali wotero. (Pano, Haji Abd al-Habib al-Attari anayamba kukumbukira amayi ake omwe anamwalira) Ndinali ku Baghdad pamene amayi anga anamwalira ku Pakistan. Banja langa linandiwuza kuti usiku omwe anamwalira, anaphika okha chakudya chamadzulo. Ngakhale panthawiyo, sanatipatse mwayi wowatumikira. Iwo ankapemphera kwa Allah Wamphanvu zonse, “O Allah Wamphanvu zonse! Musandipangitse kukhala odalira wina aliyense kupatula Inu.”

Allah Wamphanvu zonse analandira pemphero lawo. Tsopano, ndani angakhale wonvetsa chisoni kuposa munthu yemwe akhoza kutumikira amayi ake kapena atate ake, koma akunena kuti, “Okalamba awa amandisokosera”, kapena, “Kodi ndingo wngongola ndalama zambiri chonchi pa makolo anga?” Achite manyazi kwa ana otero omwe amawona makolo awo kukhala katundu! Ndi dalitso kuti chuma chathu chiwonongedwe pa makolo athu. Pajatu iwo anatiwonongera ndalama moyo wawo wonse. Chilichonse chomwe tili nacho, ulemu uliwonse, kutchuka, ndi chuma chomwe tapeza, zonsezi n'chifukwa cha dalitso la makolo athu, ndipo atate ali ndi udindo wawukulu pa zimenezi. Komabe, nkhalidwe lathu

lili moti sitimawathokozanso. Amayi anga amandidyetsa, amandipatsa chakumwa, amandigwira pafupi ndi ntima wawo, amandigulira zinthu, koma ndani amapereka ndalama kwa iwo? Ndani akugwira ntchito ndi kubweretsa ndalama kunyumba? Atate ndiye nsanamira ya banja lonse, komabe palibe amene amawathokoza kapena kuzindikira ululu omwe amapirira mwakachetechete. Iwo ndiye thandizi wa banja lonse komanso ntengo wopereka nthunzi kwa banja lonse. Munthu wosawuka amagwira ntchito molimbika, amatipatsa nthunzi, amatisangalatsa ndi khama lake, ndipo chilichonse chomwe tili nacho ndi chake. Izi sizomwe ndikunena ine basi. Izi ndi zomwe Mtumiki Wankulu ﷺ ananena. Ganizirani nkhani yodabwitsa iyi yanthawi ya Mtumiki.

Nkhani yonvetsa Chisoni ya Atate

Mwana wina anabwera kudzadandawula za atate ake kwa Mtumiki Wachifundo ﷺ. “Atate anga akufuna kutenga chuma changa”, iye anafotokoza. Mtumiki Wokondedwa ﷺ analengeza kuti, “Bweretsani atate ako pano.” Atafika, Mtumiki Wopatulika ﷺ anafunsa kuti, “Mwana wanu wanena kuti mukufuna kutenga chuma chake. Kodi zimenezo ndi zowona?” Atatewo anati, “Chonde mufunsemi zomwe ndimachita ndi ndalama zomwe ndimatenga. Kodi ndimagwiritsa ntchito bwanji ndalama zomwe ndimamupempha? Ndimazigwiritsa ntchito polandira alendo komanso kukwaniritsa zosowa za banja langa ndi ana anga.”

Pamene kukambirana kumeneku kunkachitika, Ngero Jibril ﷺ anawonekera ndipo anawulula kuti, “Ntate uyu wapanga ndime za ndakatulo mu ntima mwake koma sanazinene mokweza. Mufunsemi kuti azitchule.” Popereka nkhani za zinthu zobisika, Mtumiki Wankulu ﷺ anati, “Waganizira za ndakatulo yomwe sunanene.” Atatewo anafuwula, “Allah nthawi zonse amawonjezera chikhulupiriro chathu ndi nzeru kudzera m'zizindikiro zanu”, asanatchule ndakatulo iyi kwa Mtumiki Wachifundo ﷺ. Tanthawuzo la zimenezo ndi motere (ndipo ikufotokoza za atate akulankhula ndi mwana wake):

“Ndinakupatsa chakudya ndi kunyamula katundu wako kuyambira tsiku lomwe unabadwa. Pamene unali mwana, unadyetsedwa ndi zomwe ndinkapeza,

mobwerezabwera. Nthawi zonse matenda kapena mantha akakugwera, ndinkakhala mmaso usiku wonse kuti ndikusamalire.” “Ntima wanga unkawopa kuti ungamwalire, ngakhale ndinkadziwa kuti infa n'zosapeweka kwa aliyense. Maso anga ankallira ngati kuti matenda omwe anakugwera usiku andigwera inenso. Ndinkanva ululu, kukhala osakhazikika, ndi kukhala ndi nkhwawa.” “Ndinakulera mpaka unakulitsa mapiko ndi kufika pamalo omwe ndinkayembekezera kuti udzandithandiza, koma unandibwezera ndi ukali komanso mawu achipongwe.” “Ngati utalephera kulemekeza ufulu wanga wokhala atate ako, ukanandichitira ngati momwe munthu amachitira mnansi wake. Pamenepo, ukanandisamalira pang'ono.”

Atanva izi, Mtumiki Wachifundo صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anayamba kulira, asanagwire kolala ya mwanayo ndikulengeza kuti, إِذْهَبْ أَنْتَ وَمَالُكَ رَبِّكَ – “Pita! Iwe ndi chuma chako ndi za atate ako.”¹

Makolo amakhala ndi moyo chifukwa cha ana awo

Mtumiki Wankulu صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, “Iwe ndi chuma chako ndinu chuma cha atate ako.”

Masiku ano, ana aamuna akamapereka ndalama kwa atate awo, amati, “Atate, izi ndi zanga ndipo izi ndi zanu. Mukuyembekezera kuti ndikupatseni zingati? Chifukwa chani mukupempha mobwereza bwereza?” Atate anu sananenepo zinthu zotere pamene anakudyetsani. M'malo mwake, iye anasiya chakudya chake kuti ayike chakudya pa mbale yanu. Iwo anataya maloto awo pambali kuti akulere. Nthawi zambiri sankavala zovala zatsopano koma nthawi zonse anakugulirani zovala ndi nsapato

zatsopano. Amakubweretserani chilichonse chomwe munkapempha. Kodi tinayamba tayimapo kuganiza za nthawi yomaliza yomwe atate anu anagulirani chinachake? Kodi ananenapo kuti, “Ndinazikonda kwambiri nsapato izi, choncho ndadzigulira ndekha”?

¹ Al-Mu‘jam al-Ṣaghīr: Hadith 944

Mwina, kamodzikamodzi. M'malo mwake, atate nthawi zonse amati, “Ndinagula izi chifukwa cha mwana wanga wamwamuna”, “Ndinagula izi chifukwa cha mwana wanga wankazi”, kapena “Ndinagula izi chifukwa cha nkazi wanga.” Makolo ndi anthu odabwitsa. Sakhala ndi moyo chifukwa cha iwo okha, koma chifukwa cha ana awo.

Koma ana akakula ndikunyoza makolo awo ndikumawalankhulira mawu onyoza, taganizani ululu omwe makolowo amanva! Mabuku amafotokoza ulemu womwe atate ayenera kupatsidwa motere, “Mwana ayenera kuyima pamaso pa atate ake monga momwe wantchito amayimira

(Tafsīr Durr al-Manthūr, part 15, Banī Isrāʾīl, under verse 24, vol. 5, p. 259; Al-Mustadrak, Hadith 7345)

pamaso pa bwana wake.” Pamene atate alamula mwana wake, mwanayo ayenera kuyankha ndi, كَيْيَك. Uku ndiko kuyenera ndi ulemu womwe akuyenera. Komabe, masiku ano

nkhalidwe wayipirayipira kotero kuti mawudindo akuwoneka ngati osinthana. Mwanayo akuchita ngati bwana, ndipo atate ngati wantchito. Tsopano, atate akati, “Mwana wanga, ndikufuna ndalama”, mwanayo amakana, kunena kuti, “Ndilibe.” Kapena atate akati, “Mwana wanga, bwera kuno, ndikufuna thandizo”, mwanayo amayankha kuti,

“Ndilibe nthawi.”

Mwana yemwe anasiya atate ake

Hadith ikuti:

Allah akhoza kusankha kuchedwetsa chilango cha machimo onse mpaka pa Tsiku la Chiweruzo. Komabe, chilango chosanvera makolo chimaperekedwanso m'dziko lino, pa nthawi ya moyo wa munthu. Zotsatira zake, ngati munthu sanyalanyaza makolo ake, ana ake enieni

adzamunyoza pambuyo pake. Chochitika chodziwika bwino chimanena za mnyamata yemwe anakwatira. Atate ake anali okalamba ndipo anakakosomola

pafupipafupi.

nkazi wake anati, “N’tulutseni nkhalamba iyi m’nyumba.” Mwanayo, posonkhezeredwa ndi nkazi wake, anatenga atate ake ndikunyamuka, ndi cholinga chowasiya pamalo opanda anthu. Atatewo anati, “Mwana wanga! Kodi ukunditenga kupita nane kwinkwake mu kuzizira uku? Osachepera ndipatse bulangeti.” Mwana wosanverayo anabwera ndi mwana wake wamwamuna. Mwanayo anafuwula, “Agogo! Ndikubweretserani bulangeti.” Pamene mwanayo anabwerera, anali atadula bulangetelo pakati ndipo anabweretsa chidutsa chimodzi. Mwana wosanverayo anafunsa mwana wake kuti,

“Chifukwa chani wabweretsa theka lokha?” Mwanayo anayankha kuti, “Theka ili ndi lawo, ndipo inu mukadzakalamba, inunso ndidzakutengerani kupita nanu kwinkwake. Ndidzakupatsani theka lina panthawiyu.” Mwana wosanverayo analira pomwe anzindikira kuti zomwe anali pafupi kuwachitira atate ake, ana ake adzachichitanso kwa iye pambuyo pake.

Musayiwale chifundo cha atate anu

M’mbuyomu, tinkanva kuti nyumba zosungirako okalamba zinali ku Ulaya ndi ku America kokha, koma tsopano zikumangidwa mu Pakistan. Anthu akuyamba kuyika atate awo m’malo amenewa. Achipongwe bwanji! Ili linali khomo la Paradiso, lomwe mwalitaya kunja kwa nyumba ndikuliika m’nyumba yosamalira okalamba! Pamene atate akalamba ndikukhosomola zimakusokoserani, koma kodi munayamba mwaganizira momwe munayipitsiraira kama wanu pa nthawi yawubwana wanu, komabe panthawiyu, atate sanakutulutseni m’nyumba? Kodi munayamba mwaganizira za usiku ungati womwe atate anu anakhala maso pa nthawi yawubwana wanu? Munthu amazindikira zinthu izi pokhapokha akakhala atate iye mwini.

Pamenepo, amazindikira momwe ziliri zovuta kulera mwana. Masiku ano, pali njira zambiri zothandizira, monga matewera (diapers) ndi zina zotero. Tiyenera kuganiza za zaka 30 kapena 40 zapitazo pamene tinali ana; kodi makolo athu anatilera bwanji ndi ndalama zochepa choncho?

Mwana ndi munthu okalamba ndi ofanana Omwe ali achinyamata ayenera kukumbukira kuti pali gawo pa moyo pomwe, pambuyo pokalamba, munthu amakhala ngati mwana kachiwiri, ngati kuti moyo wabwerera kumene unayambira. Ubwana, unyamata,

ndiyeno ukalamba. Ukalamba ndi ubwana zili pamlingo umodzi. Monga momwe mwana sazindikira zinthu, munthu okalamba amavutikanso kuzindikira. Mwana ndi wowumirira, ndipo munthu okalamba amathanso kukhala wowumirira. Ngati mulingo wa kuzindikira wa mwana uli wochepe, wa munthu okalamba nawo udzachepe. Nthawi zambiri timati, “Kodi atate angakhale wowumirira choncho bwanji?” Musawaganizire kukhala wa zaka 60 kachiwiri, aganizireni kukhala wa zaka 6. Pamene mwana wa zaka 6 awumirira chinachake, ndani amatsutsana ndi mwana pa nthawi? M'malo mwake, mumanva chikondi kwa mwanayo. Ngati atate anu ali ndi zaka 60, mulingo wawo wa kuzindikira ukhoza kukhala utachepe. Tsopano, akuyenera kuchiritsidwa ndi chikondi nawonso. Pamene atate anu awumirira kapena samanva, muyenera kuzindikira kuti mukulankhula ndi mwana wa zaka 6. Poganiza motere, kutumikira atate anu kudzakhala kosavuta ndipo palibe chomwe anganene chomwe chidzakukhumudwitsani. Nthawi zambiri, nkwiyo umabwera chifukwa choganiza kuti,

“Chifukwa chani sakuzindikira zomwe ndikunena?” Muyenera kudziletsa kukwiya.

Kumbukirani, anthu osowa mwayi okha ndi omwe amachita zinthu mopanda ulemu ndi makolo awo okalamba!

Mumakolola zomwe mwazala

Zalankhulidwa kuti mwana wina nthawi ina anakwiyitsidwa kwambiri ndi atate ake. Anakonza zotenga atate ake kupita nawo ku mgalu (canal) ndikukawakankhira m'madzi. Pamene anatenga atate ake kupita nawo pa mlatho wa mgalu uja, atatewo anazindikira zomwe zinkachitika ndipo anati, “Mwana wanga,

osati pano, pita patsogolo pang'ono ndipo ukandikankhire pomwe madzi ali othamanga kwambiri.”

Mwanayo anadabwa. “Mukunena chani?”, iye anafunsa. Atatewo anayankha kuti,

“Ndinawakankhira atate anga m'madzi pamalo pomwepo. Zomwe uli pafupi kundichitira, ndizo zomwe ndinawachitira atate anga, ndipo tsopano ndikukumana ndi zotsatira za zochita zanga.”¹

M'dziko lino, timanyamula zotsatira za zochitazathu. Ana omwe amalemekeza atate awo, pambuyo pake, adzalemekezedwa m'tsogolo ndi ana awo enieni.

Ngati mwawonapo ana akupsopsona dzanja la atate awo, mufunsemi ngati iye anawalemekeza atate ake enieni. Iye ndithu adzanena kuti anatero.

Munthu yemwe amalemekeza atate ake; Allah Wamphanvu zonse adzapangitsa ana a munthuyo kukhala onvera kwa iye. Choncho, kondani atate anu, alemekezeni, ndipo musawafowoketse. Anthu ena opusa amakana kukumana kapena kulankhula ndi atate awo. Amayi amakumbatira mwana wawo mwamphanvu, kumutcha “wokondedwa wanga” ndi mawu ena achikondi. Ngakhale atate sangazitchule monveka bwino, amakonda kwambiri ana awo, ndipo ndichifukwa chake amachita chilichonse chifukwa cha iwo.

Akhoza kusanene ndi pakamwa, koma amanva chifundo chachikulu m'ntima mwawo.

¹ Jēsi Karnī Wēsi Bharnī, p. 90

Imām Aḥmad Razā Khān رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati:

"Anthu opusa, oyipa, komanso osadziwa akapeza mphanvu ndi ulamuliro, amayesera mphanvuzo kwa atate awo okalamba ndipo sanvera malamulo awo. Posachedwa, nthawi idzafika pamene iwonso adzakalamba, ndipo adzalawa zotsatira za zochita zawo.

Munthu amakolola chimene wadzala, ndipo chilango cha m'moyo wa pambuyo pa infa ndi chowopsa komanso chamuyaya." (Fatāwā Riḍwiyya, vol. 24, p. 424)

Thābit al-Bunānī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati:

"Mwamuna wina anawoneka akumenya atate wake. Anthu anamudzudzula n'kumati, 'Iwe munthu wamatsoka! Kodi ukuchita chani ichi?' Atatewo anayankha kuti,

'Musiyeni, chifukwa inenso ndinali kumenya atate anga pomwe pano. N'chifukwa chake mwana wangayu akundichitiranso chimodzimodzi. Izi ndi zotsatira za zochita zanga, musamuyimbe mlandu.' (Tanbih al-Ghāfilin, p. 69)

Ulemu kwa Atate

Zindikirani izi komanso kuyamikira chikondi cha atate anu. Nthawi zina, mwana ayenera kunena kwa atate ake kuti, “Chilichonse chomwe ndili nacho lero, n'chifukwa cha inu.” Izi ndithu zidzadzaza maso awo ndi misozi.

Ubwino wa atate potengera M'mahadith

Ena amangokhala ndi ubale wabwino ndi amayi awo

koma amakangana ndi atate awo. Izi ziyenera kupewedwa. Munthu ayenera

kuwalemekeza ndi kuwapatsa ulemu nawonso. Mtumiki Womaliza ﷺ anati, “Atate ndiye chitseko chapakati cha Paradiso.

Ndi kusankha kwanu ngati muteteza ichi kapena kuchisiya.”¹ Mtumiki Wankulu ﷺ anatinso, “Mwana sangathe kubwezera mokwanira ufulu wa atate wake, kupatula ngati atapeza atate wake ali wantchito,

n'kumugula, ndipo n'kumumasula.”²

Mfundo yofunika kwambiri yatchulidwa mu hadith ina, “Kusangalala kwa Allah Wamphanvu zonse kuli n'kusangalala kwa atate, ndipo kukwiya kwa Allah Wamphanvu zonse kuli m'nkukwiya wa atate.”³

.” Izi zikutanthawuza kuti titha kunena kuti, ngati atate a munthu asangalala naye, Allah Wamphanvu zonse wasangalala naye. Ngati atate ake amukwiya, Allah Wamphanvu zonse nayenso amukwiya.

Wina anayendera Mtumiki Wachifundo ﷺ ndipo anafunsa kuti, “O

¹ Jāmi' al-Tirmidhī: Hadith 1906

² Ṣaḥīḥ Muslim: Hadith 3799

Mufti Aḥmad Yār Khān analankhula zokhuza Hadithi:

"Nfundo yaikulu ndi yoti, ngakhale mwana atatamikira abambo ake kotalira bwanji, sangathe kubwezera mokwanira zonse zomwe abambo akewo anamuchitira. Njira yokha imene angakwaniritsire zimenezi ndi ngati mwanayo ali womasuka komanso wolemera, ndipo abambo ake ali kapolo. Mwanayo ayenera kuwagula abambowo, kuti iwo akhale Nfulu nthawi yomweyo akangowaika pansu pa umwini." (Mir' at al-Manājīḥ, vol. 5, p. 187)

³ Jāmi' al-Tirmidhī: Hadith 1907

Mtumiki wa Allah ﷺ! Ndani oyenera kwambiri kulandira khalidwe langa labwino?” Mtumiki Wankulu ﷺ anayankha kuti, “Amayi ako.”

Kenako anafunsa kuti, “Ndani pambuyo pawo?” Mtumiki Wopatulika ﷺ anati, “Amayi ako kachiwiri.” Anapitiriza kufunsa kuti, “Ndani pambuyo pawo?” Mtumiki Wachifundo ﷺ anati, “Amayi ako kachiwiri.” Anafunsa kachiwiri, “Ndani pambuyo pawo?” Pa ichi, Mtumiki Wankulu ﷺ anayankha kuti, “Atate ako.”¹

Mawu a Mtumiki Wachifundo ﷺ ali odzaza ndi nzeru. Iye ﷺ anatchula amayi katatu ndipo atate kamodzi. Chifukwa chani zili choncho? Akatswiri ophunzira za Chisilamu amati n'chifukwa chakuti amayi ali ndi zinthu zitatu zazikulu zomwe amachitira mwana wawo:

1. Amayi amanyamula mwana m'mimba mwawo kwa miyezi isanu ndi inayi.
2. Amapirira ululu wobereka.
3. Amasamalira ndi kulera mwanayo. Atate ali ndi chinthu chimodzi: amatenga

nawo mbali pakulera mwanayo. Ngakhale amayi ali ndi maufulu atatu ndipo atate ali ndi umodzi, izi sizikutanthawuza kuti munthu asamalemekeze atate ake. Akatswiri ophunzira za chisilamu analemba kuti, “Tumikirani amayi anu kwambiri koma lemekezani

atate anu kwambiri, chifukwa iye ndiye mwamuna komanso korona wa amayi anu.”²

Imām Aḥmad Razā Khān رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ analemba kuti: Ngati nkangano ubuka pakati pa makolo, ana sayenera kutsutsana ndi amayi pothandizira atate kapena mosemphana. Ana saloledwa kukangana ndi aliyense wa iwo. Muzochitika zotere,

¹ Ṣaḥīḥ al-Bukhārī: Ḥadīth 5971

² Fatāwā Riḍwīyya, vol. 24, pp. 387-390

Ulemu kwa Atate

munthu ayenera kutsatira njira ya ulemu ndi makhalidwe abwino.”¹

Mphoto ya hajj yolandiridwa pa kuyang'ana kulikonse

Kumbukirani! Amayi ndi atate

onse akuyenera ulemu wathu. Alemekezeni onse ndi kupeza mphoto ya hajj

yolandiridwa poyang'ana kwa iwo mwachikondi. Mtumiki Wachifundo ﷺ anati, “Pamene mwana wolungama ayang'ana makolo ake mwachikondi, Allah Wamphanvu zonse amalemba mphoto ya hajj imodzi yolandiridwa pa kuyang'ana kulikonse.”²

.” Mphoto ya hajj ilipo m'nyumba mwanu. Chilichonse chomwe chikusowa ndi maso achikondi oyang'anira. Masiku ano, ana amayesa kuwopseza makolo awo ndi maso awukali.³

Chisoni kwa ana omwe makolo awo amawopa kulankhula nawo. Ganizani amayi akuwopa kulankhula ndi mwana wawo wamwamuna kapena wankazi,

akuwopa kuti achitapo kanthu mwawukali kapena kumenyana. Kodi ana antunduwu ali ndi zabwino zotani? Pamene makolo anu anena chinachake, yankho lanu liyenera kukhala la ntima wonse loti بَيِّتُكَ. Uku ndiko kuyankha kumene taphunzitsidwa ndi lamulo la Chisilamu, koma ana aamuna ndi aakazi a masiku ano akulephera kuzindikira izi.

Momwe mungasangalatse makolo omwe anamwalira

Pali ambiri omwe makolo awo anamwalira ali osasangalala nawo. Pa nthawi ya moyo wa makolo awo, sayesetsa kuwasangalatsa. Ndi pambuyo poti amwalira

¹ Ibid p. 390

² Shu'ab al-Īmān: Hadith 7856

³ Mtumiki oyer a ﷺ anati,

“Aliyense amene amayang'ana abambo ake ndi maso aWukali, ndiye kuti sanawachitire zabwino.” (Tafsīr Durr al-Manthūr, gawo 15, Banī Isrā'īl, pansī pa ndime 23, vol. 5, p. 260)

m'pamene ana amazindikira zomwe achita.

Kumbukirani! Ngati atate anu asangalala, ndiye kuti Allah Wamphanvu zones wasangalalanso. Komanso, tinene kuti makolo a munthu wina anamwalira ali osasangalala naye. Akatswiri ophunzira za chisilamu anati mbadwa ziyenera kuchita ntchito zabwino zambiri, kupereka mphoto ya izi kwa makolo awo, ndikupempherera chikhululukiro chawo.¹

Kumbukirani, ntchito zabwino sizichitidwa ndi ndalama zokha, ndipo kumanga masjid si njira yokhayo yopezera mphoto. Kupereka salah ndi kuwerenga Quran yopatulika ndi ntchito zabwinonso. Ponena za ana omwe amapempherera chikhululukiro cha makolo awo mosalekeza; chifukwa cha chifundo cha Allah Wamphanvu zonse, tikukhulupirira kuti adzapangitsa miyoyo ya makolo awo kukhala yosangalala nawo, ndipo tikukhulupirira kuti adzaphatikiza ana otero pakati pa onvera.²

Momwe mungawachitire Du'a Makolo

Nthawi inakalipo. Kwa masiku anu onse otsala, onetsetsani kuti nthawi zonse mukuwapempherera makolo anu. Ndipotu, Allah Wamphanvu zonse amatiwonetsa momwe tingapempherere makolo athu mu Quran yopatulika.

وَقُلْ رَبِّ ارْحَمْهُمَا كَمَا رَبَّيْنِي صَغِيرًا ﴿٢٣﴾

(ndipo nenani kuti, “O Mbuye wanga! Achitireni chifundo (onse awiri) monga momwe anandilerera pamene ndinali mwana.”³)

Allah Wamphanvu zonse achitire chifundo makolo athu ndi kuwapatsa Paradiso! Atate anga, omwe anandigwira dzanja ndikundiphunzitsa momwe ndingayendere, anadwala kwa masiku ochepa. Sizingakhale zolakwika kunena kuti anamwalira

¹ Fatāwā Ridwiyya, vol. 24, p. 391

² Mtumiki wachifunda **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم** anati, “Amene angayendere manda amakolo awo kapena ammodzi mwa iwo lachisanu lililonse adzapatsidwa mwayi okhululukidwa komanso adzalembedwa limodzi ndi anthu ochita tchito zabwino.” (Shu’ab al-Īmān: Hadith 7901)

Quran ³ Al-, Banī Isrā’īl, vesi 24; kumasulira kuchokera mu Kanz al-‘Irfān

Ulemu kwa Atate

m'njira ya Allah Wamphanvu zonse, chifukwa anali atapita ku masjid kukapemphera. Mwadzidzidzi anagwa ndipo anavulala mmutu, chifukwa chake anatengedwa kupita ku chipatala. Sanabwerere kunyumba. Allah Wamphanvu zonse akweze maudindo awo ndi kutikhululukira popanda chiweruzo chifukwa cha iwo. Ndithudi, makolo ndi anthu akuluakulu. Allah Wamphanvu zones atipatse luso lowayamikira.

أَمِينَ بِجَاهِ خَاتِمِ النَّبِيِّينَ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Chithandizo chowonjezera rizq

Mtumiki Wachifundo صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anafotokoza kuti, “Aliyense amene akufuna kuti moyo wake ndi riziki yake ziwonjezereke azichitira makolo ake zabwino ndikusunga ubale wabwino ndi achibale ake.”¹

Chifukwa choyambitsa kusowa kwa Madalitso mu rizq

Mtumiki Wankulu ndi Womaliza صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, “Pamene munthu Asiya kupempherera makolo ake, riziki yake imadulidwa.”²

¹ Musnad Imām Aḥmad: Hadith 13812

² Kanz al-‘Ummāl: Hadith 25528

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ "اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ" بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

Mawu a Ameer Ahl al-Sunnah

"Makolo ayenera kusamaliridwa ndi chisamaliro komanso ulemu waukulu. Tiyenera kukhalanawo mwatcheru kwambiri mwakuti nthawi iliyonse yomwe akutiitana, tisiye chilichonse chomwe tikupanga ndipo nthawi yomweyo tipite kukawatumikira, kwinaku tikuyankha mwaulemu kuti, 'Eya, Mayi' kapena 'Eya, Atate.'" (Niki ki Da'wat, tsamba 437)



Faizan-e-Madinah, Muhallah Sodagaran, purani sabzi mandi, Karachi.

UAN +92 21 111 25 26 92   0313-1139278

 www.maktabatulmadinah.com / www.dawateislami.net

 feedback@maktabatulmadinah.com / ilmia@dawateislami.net